

MIYAMBI NDI MATHANTHAUZO AKE YA

GIREDI 10-12

1. KULIRIRA KUUTSI

YANKHO: Kubisa coipa kupyolera mcoipa cina.

2. LENDE N'KUKANKHANA; MNZAKO AKAKUTI KONZU, NAWWE UMAMTI KONZU; UCEMBERE NKUDYERANA.

YANKHO: Mnzako akakucitira zaufulu iwenso tsiku lina pamene waonera pafunika kumcitiranso zaufulu.

3. MASO AIPSA, KAMWA LIKONZA, MASO ALI NDI NJIRU

YANKHO: Cinthu cymene ciipa m'maonekedwe, mwina mkati mwake cimakhala konzuna ndi copatsa mphamvu.

4. KUBWERZERA PHALA KUMKOBWE

YANKHO: Mwambi woletsa kucitira zoipa anthu aticitira zabwino popeza azaleka.

5. KUTENGERA ZINTHU PAMGON'GO

YANKHO: Kungoyamba mlandu usanapeze umboni wokwanira.

6. TEKA NTALAWA ADATHA M'PHIKA

YANKHO: Coipa munthu akaciyamba pang'ono, bwino lake sadzatha kudziletsa ayi adzangopitirira.

7. MNZAKO AKAPSA NDEBVU MZIMIRE

YANKHO: Mnzathu akapezeka pamabvuto pafunika kumthandiza ndipo mwa njira imeneyi, tikhoza kuombola mnzathu ku zoopsa.

8. ULI DERE N'KULINGA UTAYENDA NAYE

YANKHO: Munthu kuti adziwane ndi mnzake pafunika kuyenda naye.

9. ULEMU WABULUZI M'NYUMBA YA MFUMU

YANKHO: Munthu wopanda ulemu akhoza kuoneka waulemu pamene akhala pakati pa anthu aulemu.

10. AKULU AKULU NDI MDAMBO MOZIMIRA MOTO.

YANKHO: Akulu akulu ndiwo ali ndi nzeru zakuya zothetsera mabvuto.

11. FODYA WAKO NDI UYO ALI PAMPHUNO:

Pafupi ndi apo wafika.
yankho: malo amene sunafikepo suyenera unena kuti m'pafupi popeza zooneka panjira palibe amene angadziwe.

12. ZAKUMZINDA SAULULA



YANKHO: Zinthu akati n'coyenera kubisa zizikhala zobisika.

13.KAPEZA ANZAKO AKUKANZINGA MASO, NAWA TONG'OLA AKO.

YANKHO: Pali pofunika kumacita nawo nawo zinthu monga eni mudzi acita.

**14.PAMUDZI PAKAKHALA PAZITSIRU MKAMWINI
ASAMAKULIRAPO MWENDO: APAWO NDI MIZU YA
KACHERE IKUMANA PANSI.**

YANKHO: Munthu ukakhala pamudzi paeni pafunika kuwalemekeza ngakhale n'ngopanda nzeru./ Mkamwini asamazitama pena kuzitamandira.

15.KUMERA M'KHOLA MSIPU: MSIPUWAMERA M'KHOLA

YANKHO: Zinthu zimene zimapezeka patali ndipo mobvutira, tsopano ziri kupezeka patali ndiponso mopanda mabvuto.

16.KUOLOKERA PA KANGAUDE

YANKHO: Kupulumuka pa milandu cifukwa ca kandale kakang'onong'ono.

17.KUTHAWA MTSWATSWA WAKO WOMWE

YANKHO: Kukana cinthu comwe wacita iye mwini.

18.NGUWO YOBWEREKA SILIMBA MTHUPI

YANKHO: Munthu asamanyadira kanthu kobwereka popeza mwini wake amangobwera mwadzidzidzi kudzatenga.

19.KUZINGWA KWA KALULU KUKAPSA

YANKHO: Kusauka kwakukulu.

20. SAYENDA ADABALA MWANA ADAYENDA

YANKHO: Mwambi wophuunzitsa kusacitira coipa anzathu popeza zoipa zathu zingadzagwere ana athu.

21.CINASALA CIDAKANIKI FISI

YANKHO: Munthu akaleka cinthu akadacikonda cimene adazolowera, tsiku lina amadzabwerera kucomweco.

22.UKALEMERA UMayankhulira M'CIGULU

YANKHO: Munthu akalemere azingodziwa yekha za Cuma cake popeza akauza anthu ena, tsiku lina adzauza akuba ndipo adzamubera.

23.KUCHERA NDIWO N'KUWERAMA

YANKHO: Munthu ayenera kucita zinthu mofulumira ndiponso kulingalira mwanzeru.

24. UKAKHALA MWANA, MPHANE UMayambira Pamcenga.

YANKHO: Munthu ayenera kugwira nchito molingana ndi monga angathere.

25. PASAMBIRA MFULU KAPOLO ASAMBIRA POMWEPO.

YANKHO: Kawiri kawiri mwayi wa mfulu umafikiranso kwa anthu wamba.

26. KUYENDA NKUBVINA.

YANKHO: Munthu asamacita za upandu navesa kuti sadzadz ziwika popeza nthawi imene sayembekeza iye, mphulupulu zake zimafululika tsiku lina.

27. KUMANGA KHOBWE NDI M'MAWA

YANKHO: Munthu amene amacedwa pa nchito sapindula.

28. MWEZI SATUNGIRA MKANDA

YANKHO: Zinthu zocitira mumtima sidzicitika bwino.

29. KUDZA KWA MAFINYA NDI MUNGA WOMWE

YANKHO: Kupezeka kwa zinthu ziwiri zomwe amafuna panthawi imodzi.

30. KUPHA NJOKA NKUDULA MUTU: KULANGA NYANI

NKUPHWANYA MUTU.

YANKHO: Njira yoziziritsiramo mabvutondi kulondola cymene cidautsa bvutolo ndi kucicotsa.

31. AKAPSALA SAPI SANA M'MATUMBA: AKPSALA SAMETANA AOPA KUCEKANA.

YANKHO: Anthu oenjera akadziwana sangathe kucenjererana.

32. ZILIKO LINGA UTATOSAKO

YANKHO: Mwambi wophunzitsa munthu kusaneneratu asanapeze momwe mlandu unaliri.

33. KWA ENI KULIBE MKUWE

YANKHO: Cimakhala cobvuta kwa mlendo kupambana mlandu mdziko la eni.


34. KUTEMETSA NKHWANGWA PA MWALA

YANKHO: Kukana molimba ndi motsimikiza.

35. UFULU WANG'OMBE WOKWETEZA MCIRA

YANKHO: Kuona anthu olemera ngati alibe mabvuto.

36. KUTAYA UDZU WOMWETAMWETA



YANKHO: Kutaya cabwino uli naco poganiza kuti mwina
sicidzakuphindulira.

37.KHASULA APONGOZI LOPANDA MBETETE.

YANKHO: Cinthu camwini sikotheka kucigwirira nchito monga mmene
udazolowerera kugwiritsa nchito cakocako.

38.UKO KULIRE N’KUMTSUKWA

YANKHO: Njira yodziwirammo wamng’ono.

**39.WOLUKA NSENGWA ADYERA M’CIPAPA: WOSOKA MPHASA
AGONERA PA ZIDUTSWA: WOUMBA MBIYA APHIKIRA
M’PHALE.**

YANKHO: Kawiri kawiri munthu amacita kaso ndi zake ndipo sakonda
kuigwirira nchito.

40.GONA NDI MWINI WAKE NYUMBA

YANKHO: Ulamuliro wa cinthu uyenera kucokera kwa mwini cinthuco.

41.KWAGWERA MTENGO WANTHAMBI SIKUSOWA

YANKHO: Anthu omveka kapena olemera akacita cinthu, cinthuco
cimamveka patali.

42.UKAKHALA WOPANDA CALA USAMADANA NKULOZA.

YANKHO: Ngati ulibe cinthu usamadana ndi ajaali nazo.

43.KANTHU NKAKO UBVUNDUKULA NUPENYA.

YANKHO: Cinthu cako cako ndico cabwino cifukwa ucita ndi mtima
wokhaikika nucita cifuniro cakonso.

44.KANTHU N’KAVUMBU KADAVUMBULA MENDE PACHISA.

YANKHO: Zinthu zadzidzidzi zimautsa zinthu zagonire zimene zinali
zobisika.

45.KALULU ADATUMA NOBVU

YANKHO: Njira yotumirammo munthu wamkulu mwaulemu.

46.KUMVA ZAM’MALUWA

YANKHO: Mwambi wakuletsa kunena nkhani zomwe sunamve bwino
bwino.

47.KUDZIWANA NKUTHERA THUMBA LAMCERE PAMODZI.

YANKHO: Anthu amene akhala pamodzi nthawi yaitali ndiwo amene
akhoza kudziwana.

48.KUCULUKANA NKWABWINO KUIPIRA KUTHETSA MCERE.



- YANKHO: Panchito mukaculuka imacitika msanga ngakhale kuti cakudya cimatha msanga.
- 49.KUGONA PAKATI NKUYAMBIRIRA.**
YANKHO: Munthu afunika kucita cangu panchito kuti apeze mtendere patsogolo pake.
- 50.MBALAME ZOMWERA CIGOBI CIMODZI ZIDZIWANA NTHENGA.**
YANKHO: anthu amene amadyera, khala kapena kukambirana ndiwo amadiwana kweni kweni
- 51.KUENJEZA CA MPHONGO**
YANKHO; Woletsa kucitira zoipa munthu amene aticitira zabwino.
- 52.KUOMBERANA MAPIRA PAMUTU**
YANKHO; Kupeza mwai kaamba ka mphamvu za ena.
- 53.KUONERANA MKODI: KUONERANA M'MADZI**
YANKHO: Kusungirana coipa kumtima.
- 54.FISI AKAGWA M'MBUNA SAYANKHULAKANTHU.**
YANKHO: KAWIRI Kawiri munthu amene amvera zonsezimene mtima wake umulamulira, sayenera kudabwa pamene apezeka kuti wagwa m'zobvuta.
- 55.CADODOMETSA MLEME CIRI NDI KHAMBI:CALAKA NYANI CIRI NDI KHAMBI.**
YANKHO: munthu wokonda njira zakuti zakuti ndiye akazileka ndiye kuti pali calengetsa.
- 56.MWANA AKALIRA NYANGA YAMTSATSI M'SEMERE MFOTERE YEKHA M'DZANJA**
YANKHO: Munthu ngati safuna kumva zomuuza anzake koma kumuleka ndipo akapezana ndi mabvuto, amazindikira yekha naphunzira phunziro limene sadzaliwalanso.
- 57.ZACOKA NDUNDU TIYANIKEKO INSWA: PA UNYINJI SABUULILAPO.**
YANKHO: Mwambi wonenedwa pamene mufuna kukamba za cisinsi ngati ena amene sanayenera kumva akacokapo.
- 58.CIMANGA CILOLA OPANDA MANO**
YANKHO: Nthawi zambiri mwayi umagwera amene alibe nawo nchito kweni kweni.

59.CIZOLOWEZI CA NAMKHOLOWA CIDAULULITSA MBATATA

YANKHO: Munthu akamacita cizolowezi ndi zinthu zazing'ono, tsiku lina zazing'onozo zidzakamuitanira z azikulu.

60.MWANA WAPANG'OMA SALEPHERA KUYANGALA.

YANKHO: Munthu amene ali ndi luso lakuti lakuti, mwana amakhalanso wa lusolo.

61.NKHWANGWA IKAGWA PAMADZI DZANJA POMWEPO.

YANKHO: Mwambi wophunzitsa kusacedweka mlandu poopa zobvuta zina omwe zingatsaire ngati ticedweka.

62.NKHWANGWA YOBWEREKA SIKHALA KUGULUKA:

NKHWANGWA YOBWEREKA SIKHALA KUSWEKA MPINI.

YANKHO: Cinthu cobwereka munthu sacedwa kucita naco ngozi.

63.CIRI KUMNZAKO N'KUMATI CIGWIRE NYANGA.

YANKHO: Mabvuto ali kumnzako umayesa kuti simabvuto eni eni koma pokhapo pamene ali kwa iwe.

64.KUM'KIRA NSALE N'KUMODZI

YANKHO: Anthu ngati akondana kwambiri, zocita zawo zimakhalanso zofanana.

65.CIKONDI CACOTSA PHAZI M'PONDEPO

YANKHO: Anthu okondana kwambiri, makhalidwe awo amafanananso.

66.MAU ALI POYAMBA OTSIRIZA M'MANG'OMBE

YANKHO: Pokamba nkhani anthu amamvera mau oyamba.

67.MWINI PHALE SAKUDA CALA

YANKHO: Munthu waubve sadziona kuti ndi waubve angoti kukhala nkumeneku.

68.UTISOKOSERA NKULINGA UTAMVA.

YANKHO: Ciriconse cymene munthu atiuza,tisamayambe kunyoza ayi popeza mwina tidzanyalanyaza mau otiombola ife.


69.KUYENDA NDI KUSERI KWA PHAZI: KUYENDA NDI KUMSANA.

YANKHO: Cikondwerero coposa cikondwerero conse.

70.PAGULE FUMBI NDIWE MWINI.

YANKHO: Munthu ali ndi anchito, iyeyo ayenera kuyamba kugwira nchito molimbikira ndipo anchitonso adzatola citsanzo comweco.

71.MWANA WA MNZAKO N'KASAMBE WAKO N'KAZIDYA

- 
- YANKHO:** Mwambi wongotidziwitsa za mitima yoipa ya azimai ena.
- 72.CIMVANO CA MABVU CONING'A PAMIMBA**
- YANKHO:** Mwambi wotiphunzitsa kutengerako cimvano cotere.
- 73.PAPITA MNJERE MPENI UPITA POMWEPO**
- YANKHO:** Pamene munthu tsoka laling'ono likamgwera patsogolo pake tsoka lalikulu limadamgweranso munthu yemweyo.
- 74.MVULA IKAKUONA LITSIO SIKATA**
- YANKHO:** Mabvuto akayamba kukubwerera salekeza amangobwererabwererabe.
- 75.KANTHU KALI MUNYE: KANTHU KALI KUCALA**
- YANKHO:** KUcokera mwa munye (cala comwe munthu amalozera naco), tikhoza kudziwa zinthu zmbiri.
- 76.MWANA WANG'ONA NDI UYO ALI PAMCIRA**
- YANKHO:** Kcenjeza ana kuti ayenera kutsatira zimene makolo awo acita.
- 77.MWANA WANG'ONA SAAKULIRA DZIWE LIMODZI.**
- YANKHO:** wokambidwa ndi anthu aulesi oleka leka nchito.
- 78.TSOKONOMBWE ADATHA DZIKO NKULUMPHA.**
- YANKHO:** Mwambi wonenedwe ndi omwe amagwira nchito pang'on pang'on podzilimbikitsa.
- 79.ODWALA AGAWA M'PHIKA**
- YANKHO:** Mwambi wonyoza ndi kutsukuluza munthu amene apezeka pa zabwino pokha pokha koma pazobvuta sapezeka.
- 80.MTHENGO MUDALAKA NJOKA**
- YANKHO:** Munthu pocoka pa mudzi asamanyoza popeza nkwapafupi kubweranso.
- 81.CULUKE CULUKE NGWA NJUCI UMANENA IMENE YAKULUMA**
- YANKHO:** Ndi mwambi wonenedwa pofuna kudziwa amene wabweretsa bvuto.
- 82.ZATHU SALOWA MKHOLA**
- YANKHO:** Cuma ca anthu ambiri, umodzi sakhoza kucita naco m'mene afunira.
- 83.KUTOLA NKHWANGWA NDI MPINI WOMWE**
- YANKHO:**Kupeza zinthu ziwiri zomwe mafuna kwambiri panthawi imodzi.

84.DZIKO MMAFUWA ACITA KUCIRIKIZA.

YANKHO: Anthu mdziko ngati akhala bwino, Dziko limakhalanso pa mtendere.

85.MADZI AKATAYIKASAOLEKA

YANKHO:: Munthu asamataya nthawi pazinthu zataika koma kupeza njira yopezeramo zina.

86.PHWITI AKAKHUTA SALAWIA MTONDO

YANKHO: Mwambi wophunzitsa kuyamikira pamene ena aticitira zabwino.

87.TIKONZE TIKONZE ADANYULA MALIRO YA ENI.

YANKHO: Munthu usanacite kanthu kulibwino kuyamba kufunsa.

88.ANTHU NDI MIYALA SAKUKUTIKA: ANTHU NDI MIYALA SAUNDIKA: ANTHU NDI MCENGASAUNDIKA

YANKHO: Anthu alibe mapangika.

89.CALAKA BAKHA NKHUKU SINGATOLE

YANKHO: Cimene wacilephera munthu wamphamvu, munthu wopanda mphamvu sangacithe.

90.KHWANGWALA WAMANTHA ADAFA NDI UKALAMBA: PHUKUSI LAMOYO SAKUSUNGIRA NDI MNZAKO.

YANKHO: Munthu aliyense ayenera kukhala mlonda ndi woyang'anira moyo wake.

91.UKAYENDA MCHIRE WAYENDERA ZONSE

YANKHO: Kuli bwino kupeza theka la cymene umacifuna kuposa kuungobwera wopanda mpang'ono ponse.

92.KUONGOLA MTENGO MPOYAMBA

YANKHO: Kumakhala kosatheka kuongola mwana atakula koma akali wamng'ono.

93.MADZI SAIWALA KHWAWA

YANKHO: Munthu wokonda njira zakuti zakuti, akadzileka ngakhale papite zaka zambiri amazadzikumbukiranso.

94.MTENGO UMAGWERA UKO UDAWERAMIRA

YANKHO: Zocita zamunthu zimaweramira kumene mtima wake udaima.

95.KADZIWA MWINI MKHUTO WAFULU

YANKHO: Kulibe Munthu angathe kudziwa za Munthu wina koma mwiniyo.

96.PAKADAFNDA PADAJIWITSA GALU

YANKHO: Munthu ngati samvera malangiizo a anzake, amazapeza mabvutopatsogolo pake.

97.NJUCI ZIKACULUKA SIZIIKA UCHI

YANKHO: Anthu akaculuka panchito mwina nchito simaoneka bwino.

98.NKHANGA ZINAPANGANA KUSANAPSE

YANKHO: Cinthu coopsa cisanabwere, pamafunika kupanganiranatu.

99.CAKUDZA SICIIMBA NG'OMA.

YANKHO: Munthu ayenera kukhala wokonzekeratu tsiku ndi tsiku kuti acinjirize zinthu zake.

100. MUTU UKAKULA SULEWA NKHONYA:

YANKHO: Munthu akakhala wamkulu sangathe kulewa mabvuto.

101. KUNONG'ONEZABONDO

YANKHO: Kudzitsutsa wekha pambuyo pa kugwa m'mabvuto kaamba kosamvera.

102. KUIMBAMWIYO

YANKHO: Kutanthitsa-tanthitsa mapangano osatsimikiza kucita kanthu keni-keni msanga.

103. KULASA MTENGO N'CAMUNA COMWE

YANKHO: Amenewa ndi Mau amene amanena Anthu omwe mlandu wawatsutsa pomwe amayesetsa kukamba Mau oti mlanduwo usawatsutse.

KWATHA

/dml. 2019

